

# KUIKIDWA MMANDA



Atate Akumwamba Odala, ndi a—Kukhalapo kwa Mzimu Woyera kumene kulipo kale pano, ife tikuyandikira Mawu Anu Woyera. Ndipo ngakhale ndi mawu oipa kuyesetsa kuti ndiwagwire, ndi kuwayankhula mawuwo pang'ono pang'ono basi ndi modekha momwe ine ndingathere, ine ndikupempha kutsogolera Kwanu kwa Umulungu ndi kuvomereza kwa Mzimu Woyera kuti ziyende pakati pathu usikuuno. Ndipo mulole Iye Amene ali wopezeka ponseponse, mulole Iye awatenge Mawu a Mulungu ndi kuwapereka Iwo ku mtima uliwonse, basi monga mwakusowa kwathu. Mulole Iye atidyetse ife usikuuno, pa zinthu zabwino za Mulungu.

<sup>2</sup> Ndipo usikuuno, pamene ife tikuyankhula pa Mawu, mulole mitima yathu ipite mamailosi ochuluka kupita ku Kalvare, kumene Yesu analipira mtengo wokwanira mu zonse uja umene unkafunikira wa ziweruzo zazikulu za Mulungu, kuchokera mmunda wa Edeni. Ndipo lero mulole ife tizindikire kuti ife tinalungamitsidwa mwaulele ndi chiukitsiro Chake, ndi imfa Yake, kuikidwa mmanda, ndi chiukitsiro.

<sup>3</sup> Ndipo usikuuno ife sitirinso a mdziko lapansi, pakuti ife tagulidwa ndi mtengo wa Magazi ofunikira a Mwana wa Mulungu. Ndipo mulole ife, ndi mitima yoyamikira, titembenekire kwa Inu usikuuno, ndi malingaliro onse ndi mphamvu, ndi zimene ife tiri nazo mkati mwathu, ndi kukutumikirani Inu ndi mtima wangwiro, wosadetsedwa.

<sup>4</sup> Perekani usikuuno, Atate, ngati pangakhale ena pano amene sakukudziwani Inu, mu kukhululukira kwa machimo awo, mulole iwo usiku uno abwere modzichepetsa ku mtanda, ndipo pamenepo akalape machimo awo kwa Mulungu yemwe ali wolungama, kuti akhululuke. Ndipo mulole uno ukhale usiku wopambana kwa ife tonse. Ife tikupempha izi mu Dzina la Mwana Wanu, Ambuye Yesu. Amen.

<sup>5</sup> Tsopano ife tikuzindikira kuti palibe mmodzi aliyense, pa dziko lapansi, amene ali ndi kuthekerera kokwanira kuti awatenge Mawu a Mulungu ndi kuwaulula Iwo, chifukwa Mawu analembedwa mwa kuzodza. Mzimu Woyera ndi Mlembi wa Mawu.

<sup>6</sup> Ndipo pamene mmodzi anafunidwa, Kumwamba, kuti atenge Bukhu ndi kuti amatule Zisindikizo, sanapezeke mmodzi aliyense Kumwamba, ngakhale pa dziko lapansi, ngakhale pansu pa dziko lapansi, amene anali woyenera kumatula Zisindikizo, kapena ngakhale kuyang'ana pa Bukhulo. Ndipo pamenepo panali Mwanawankhosa Apo yemwe anali ataphedwa chikhadzikitsireni maziko a dziko lapansi, ndipo Iye anabwera

ndipo anadzatenga Bukhu kuchokera mdzanja la Iye amene anakhala pa Mpandowachifumu, ndipo anamasula Zisindikizo ndipo anatsegula Mawu.

<sup>7</sup> Ndipo ife usikuuno tikukhulupirira ndi kudalira mwa Iye, kuti Iye atitsegulira ife Mawu, ndipo tsopano pamene ine ndikuwerenga mu mutu wa 2 wa Machitidwe.

<sup>8</sup> Pamene ine ndikupereka, usiku woyamba unali *Kubwera Kwachiwiri*, ndipo . . . kwa Ambuye Yesu, pokhala Lachitatu. Ndipo Lachinai usiku unali pa *Nsembe Yokwanira Mu Zonse*. Ndipo Lachisanu usiku tinali pa *Chitetezero Chokwanira Mu Zonse; Changwiro*. Kodi inu munazimvetsa izo usiku watha? *Changwiro*, momwe ife tingakhalire mwamtheradi opanda chilema ndi angwiro pamaso pa Mulungu! Ndipo usikuuno ndi pa *Kuikidwa Mmanda*. Ndipo mawa, *Chiukitsiro*. Basi monga mmene masiku akutsatirana.

<sup>9</sup> Tsopano ine ndasankha usikuuno, kuwerenga kwanga kwa Lemba, kuchokera mu Bukhu la Machitidwe, mutu wa 2 ndipo ndime ya 25, ya 26 ndi ya 27, kuphatikiza. Ndipo Iwo akuwerengeka monga chonchi, Petro akuyankhula.

*Davide, pakuti Davide anayankhula zokhudza iye, Ine ndinawona Ambuye nthawizonse pamaso panga, pakuti iye amakhala padzanja langa lamanja, kuti ine ndisasunthike:*

*Mwa ichi unakondwera mtima wanga, ndipo linasangalala lirime langa; komanso thupi langa lidzapuma mchiyembekezo:*

*Chifukwa inu simudzasiya moyo wanga mu gehena, komanso simudzalola Mmodzi Woyera wanu kuti awone chivundi.*

<sup>10</sup> Ndi mutu wokongola bwanji wa usiku uno, kuti titengepo phunziro la Iye ali mmanda.

<sup>11</sup> Chinthu choyambirira chimene ife tikufuna kuti tichiwone . . . kukoperako tcheru chanu, ndi kusalephera kwa Mawu a Mulungu. Mulungu amasunga Mawu Ake, ku lemba. Ndipo usikuuno ife tikufuna kumangitsa malingaliro athu pa zimenezo, kuti Mulungu amasunga Mawu Ake. Ife tikhoza kukhala otsimikizika za chirichonse chimene Mulungu wanena mu Mawu Ake, kukhala Choonadi. Ndipo chikhulupiriro sichimakhazikika pa mchenga wotitimira wa malingaliro a munthu kapena mbalume za munthu, koma icho chiri ndi malo ake okhazikika opumulirapo pa Thanthwe losasunthika la Mawu a Mulungu a Muyaya.

<sup>12</sup> Mawu! Ngati Mulungu anawanena iwo, iwowo ndi kwanthawizonse Choonadi. Iye sangakhoze kuwabweza iwo ndi kuti, “Ine sindimatanthauza zimenezo.” Ine ndikhoza kunena zinthu ndipo inu mukhoza kunena zinthu, tikatero ife timakhala

ndi chizolowezi chowabweza iwo, chifukwa ife tinawanena iwo mwa kupambana kwa kudziwa kwathu ndi mwa kupambana kwa kukhoza kwathu. Koma, ndiye, Mulungu ndi wosiyana kwambiri ndi ife. Iye ndi wopandamalire, chotero Iye samanena chinthu chimodzi pokhapokhapo icho chitakhala mwamtheradi changwiro. Iye samayenera kubweza icho, samasowa kuti apepese chifukwa cha chimene Iye wanena. Icho nthawizonse chimaima, Choonadi.

<sup>13</sup> Ngakhale kwa Yesu, mu masiku opambana ano amene ife tiri mu chikondwerero, pamene Mulungu anamupha kwenikweni Mwana Wake chifukwa cha machimo a dziko lapansi, zinali mwinamwake zikwi za zaka ngakhale maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe nkomwe. Mulungu anayankhula Mawu, ndipo Iwo amakhala chinthu chomalizika Kumwamba pamene Mulungu awayankhula iwo; izo zimakhala kuti zatha kale. Oh, ngati ife titangokhoza kugwira chimene icho chikutanthauza, ife tikanakhala anthu osiyana bwanji! Kuwona mu Mabukhu Ake, ziweruzo zimene zaikidwa umu za wosamvera, izo zikanamupagitsa munthu kudzifufuza yekha, ora ndi ora; ndipo izo zingawapangitse olungama kusangalala, ora ndi ora, kuwerenga madalitso amene Mulungu wawalonjeza kwa okhulupirika. Ndipo ife tikhoza kukhala otsimikiza kuti Mawu aliwonse adzakwaniritsidwa, tingozika solo yathu pamenepo. Nthawizonse zakhala ziri mwanjira imeneyo.

<sup>14</sup> Pamene Mulungu anayankhula kwa Nowa, kumbuyo uko mu dziko la chigumula; mwinamwake Baibulo lisanalembedwe nkomwe, kapena Baibulo ili, mulimonse, lisanalembedwe nkomwe; Mulungu anamuza Nowa kuti kumabwera nkuntho, ndipo madzi adzaphimba dziko lapansi. Ndipo popanda dontho limodzi la umboni kuti izo zikanadzachitika, chirichonse chinali mosiyana kwambiri, Nowa anayenda ndi mantha, ndipo anasema chombo, anachikonza icho. Icho chinali chopulumutsira a pa banja ake ndi iyemwini. Mulungu sanamukhumudwitse iye, chifukwa iwo anali Mawu Ake. Iwo ankayenera kuti achitike pamene Mulungu ananena kuti iwo akanati adzachitike.

<sup>15</sup> Tsopano, pamene Yobu, Bukhu lakale kwambiri mu Baibulo, limene linalembedwa mwinamwake Genesis asanalembedwe nkomwe, ndipo ilo linaikidwa mu Baibulo. Ndipo Mose analembe Genesis. Yobu, mu Bukhu lake, iye amakhazikika mwaulemu pa lonjezo limene Mulungu anamupangira iye. Ndipo iye amaima pambali pa nsembe yake yopysereza, wopanda mantha mu mtima mwake; akudziwa kuti, chimene Mulungu anali atachinena, Mulungu anali wothekera kuti achikwaniritse. Ndipo pamene chirichonse chinkawoneka kuti chikuyenda motsemphana, Yobu anaima mokhazikika chifukwa lonjezo la Mulungu linali lokhazikika. Mulungu anamulonjeza Yobu, ndipo Yobu anakhazikika pa lonjezo limenelo.

<sup>16</sup> O, ngati mpingo ungafike konse pa malo amenewo pamene iwo ukhoza kukhazikika mwaulemu pa Mawu a Mulungu a Muyaya kukhala Choonadi! Pangakhale kusinthika bwanji, pangakhale kukonza bwanji pamenepo, pangakhale kudula bwanji pamenepo, pangakhale chimwemwe chotani pamenepo, pangakhale mphamvu bwanji pamenepo, pamene amuna ndi akazi angamutenge Mulungu pa mtengo weniweni, chimene Iye wanena ndi Choonadi. Ziribe kanthu mmene zikuwonekera zochitika, zimenezo ziribe kanthu kochita ndi izo. Mulungu ananena chomwecho; izo zikukhazikitsa izo!

<sup>17</sup> Ndipo Yobu, pamene iye anali mu nthawi ya kuyesedwa kotheratu kwa chomuchitikira chake chonse; pamene iye anali atapezeka, mu Kukhalapo kwa Mulungu, kuti anali munthu wolungama. Ngakhale Mulungu anati iye anali wangwiro. Panalibe aliyense wonga iye pa dziko lapansi. Ndipo Satana anapatsidwa mwayi woti amuyese iye, anati, “Ine ndimupangitsa iye kuti akutukwaneni Inu pamaso Panu.”

<sup>18</sup> Ndipo iye anatsala pang’ono kuti atenge moyo wa Yobu, ndipo iye akanatha kuchita zimenezo, koma Mulungu anaika mzere wamalire, anati, “Iwe ukhoza kuchita chirichonse kwa iye, koma usatenge moyo wake.”

<sup>19</sup> Ndiye pamene Yobu anadzaima pa kuyesedwa kumene pa mphindi yovuta, iye anati, “Ine ndikudziwa Muwomboli wanga ali moyo, ndipo pa masiku otsiriza Iye adzaima pa dziko lapansi. Ngakhale mphutsi za mthupi zitawononga thupi ili, komabe mu mnofu wanga ine ndidzamuwona Mulungu.” Zinalibe kanthu kuti kumawoneka kwa mdima chotani, ndi mmene kumawonekera kuti si zenizeni, panali chinachake chimene Yobu anazikapo solo yake, lonjezo la Mulungu la Muyaya. Oh, ngati ife titangotha kuchita zimenezo! Zindikirani, iye anali kukhazikika pa lonjezolo, “Ine ndikudziwa Muomboli wanga ali moyo.”

<sup>20</sup> Ndipo ine ndikufuna kuti inu muzindikire, kwa mawu amtsogolo amene ine ndikufuna kuti ndinene, Yobu ananeneratu za malo ake odzaikidwa. Ndipo pamene Yobu anafa, iye anaikidwa pomwepo.

<sup>21</sup> Panali munthu wina, dzina lake Abrahamu, amene anamutenga Mulungu pa Mawu Ake. Ndipo iye anamukhulupirira Mulungu. Ndipo iye anadzitcha zinthu izo zimene zinali zotsutsana ndi lonjezo limene Mulungu anamupatsa iye, ngati kuti izo panalibepo. Iye anamutenga Mulungu pa Mawu Ake. Ndipo pamene masiku anadutsa, ndi masabata ndi miyezi, ndipo angakhale zaka zinadutsa, izo sizinamuchititse mantha Abrahamu mpang’ono pomwe. Baibulo linati, “Iye sanadzandime, kudzera mu kusakhulupirira, pa lonjezo la Mulungu; koma anali wokhulupirika, akupereka matamando kwa Mulungu.”

<sup>22</sup> Pamene chirichonse chinkawoneka chomwecho, tsiku lililonse, izo zimakhala zikukula movutira kwambiri tsiku lililonse; koma mmalo mofookera, Yobu amakhala wa mphamvu tsiku and tsiku. Oh, ndi chitsimikizo chodala bwanji chimene ife tiri nacho! Pamene zovuta zikuwoneka kuti zikukwera kuti zikapange chinthucho, chimene Mulungu analonjeza, chosatheka; mmalo mochita mantha, kubwerera ku dziko lapansi, ife tikuyenera kuima molimba kwambiri kuposa momwe ife tinayamba taimirapo, pa PAKUTI ATERO AMBUYE. Izo zikuyenera kukhazikitsa izo, pamene Mulungu akunena chinachake.

<sup>23</sup> Ndipo Abrahamu anadzitcha zinthu zimenezo zimene zinali, ngati kuti izo panalibepo, chifukwa izo zinali zotsutsana ndi Mawu. Ndipo pamene Abrahamu anataya wokondedwa wake ndi mkazi, Sarah, atatha kukhala limodzi zaka zambiri, iye anagula gawo la malo pafupi ndi pamalo kumene Yobu anaikidwako, ndipo anakamuikapo Sarah. Mukudabwa chiyani? Iwo anali aneneri! Iwo amawona! Iwo amakhudzana naye Mulungu! Ndipo tsopano pamene Abrahamu anafa, iye anaikidwa mmanda limodzi ndi Sarah.

<sup>24</sup> Tsopano, iye sanafune kuti anthu awa amupatse iye gawo ilo la malo. Iye anagula ilo, pamaso pa mboni. Ndi choimira chokongola bwanji cha ubatizo. Iye anagula iwo, pamaso pa mboni, kuti iwo anali cholowa chake. Oh, umo ndi momwe wokhulupirira weniweni akuyenera kubwerera, osati kungozembera pa kona, koma kudzaima pamaso pa mboni, “Ine ndine mboni ya Ambuye Yesu, ndi ya Mzimu Woyera, ndi ya ntchito Zake zazikulu,” ndipo mochulukwa kwambiri pamene ife tikuwona tsiku loipa ili likuyandikira.

<sup>25</sup> Ndiyeno pamene mwana wa Abrahamu, amene anali Isaki, lonjezo linali kuti lipatsidwe kwa iye. Ndipo pamene Isaki anafa, iye anaikidwa mmanda limodzi ndi Abrahamu. Ndipo Isaki anabala Yakobo.

<sup>26</sup> Ndipo pamene Yakobo anali. . . anakafera komwe uko mu Igupto. Koma zindikirani, iye asanafe, iye ananena kwa mwana wake mneneri, Yosefe, “Bwera kuno, mwana, ndipo uyike dzanja lako pa ntchafu yanga yolumala.” Pakuti kumbukirani momwe iye analumalira, ndi chifukwa chakuti Mngelo wa Ambuye anadzakhudza ntchafu yake, ndipo iye anatsimphina kuyambira tsiku limenero. Iye anati, “Ika dzanja lako pa ntchafu yanga, ndipo ulumbire kwa ine mwa Mulungu wa atate athu, kuti iwe sudzandiika ine kumusi kuno mu Igupto.” Chifukwa chiyani? Oh, iwo anali ndi Mawu, iwo anali ndi vumbulutso!

<sup>27</sup> Ndipo mundilole ine ndiimikire apa, kuti ndinene kuti mpingo wa Mulungu wa moyo wamangidwa pa vumbulutso la Umulungu; osati pa chipembedzo, mabungwe, osati pa

tizikhulupiro kapena ziphunzitso, koma pa Choonadi choululidwa mwauzimu cha Mulungu wamoyo.

<sup>28</sup> Abele, mmunda wa Edeni, anali nazo izo pamene mpingo unkayamba. Iye anadziwa bwanji kuti abweretse mwanawankhosa? Nchifukwa chiyani iye sanabweretse zipatso monga Kaini anachitira? Koma izo zinaululidwa kwa iye!

<sup>29</sup> Yesu nthawi ina akuyankhula, anati, “kodi anthu amati Ine Mwana wa munthu ndine ndani?”

“Ena amati Inu ndi ‘Mose,’ ndi ‘Eliya,’ zina zotero.”

Iye anati, “Koma inu mumati Ine ndi Ndani?”

<sup>30</sup> Inu mwaona, izo sizikukhazikika pa chimene winawake akuganiza, ndi chimene iwe ukudziwa kuti ndicho Choonadi. “Kodi *inu* mukuti chiyani?” Funso limenelo likhoza kukumanizana ndi mmodzi aliyense wa ife pa nkhope usikuuno, “Kodi inu mukuti chiyani?”

<sup>31</sup> Ndipo Petro mwamsanga akuyankhula, popanda kujejema kumodzi, anati, “Inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo.”

<sup>32</sup> Monga Yesu Amene ankadziwa zinsinsi za mitima yonse, pakuti Iye sanali wina koma Yehova akuwonetseredwa mu thupi, ndipo Iye anati, “Wodala ndi iwe, Simoni, mwana wa Yonasi, pakuti thupi ndi mwazi sizinaulule izi kwa iwe, koma Atate Anga amene ali Kumwamba achita izi. Ndipo pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizidzawulaka Iwo.”

<sup>33</sup> Ndipo ife anthu pamene ife tikubwera, ife Achilutera timafuna kuyenda mwa chikhulupiro, ife Amethodisti timafuna tifuule kuti tipeze Icho, inu Achipentekoste mumafuna kuyankhula ndi malirime kuti mupeze Icho, koma izo ndi mamailosi teni milioni kwa Icho.

<sup>34</sup> Icho ndi vumbuluto Laumulungu la Ambuye Yesu Khristu, Umunthu wa Thunthu Lake ukuwonetseredwa mu mtima, “Pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizidzawulaka Iwo.” Izo zimagwira ntchito mwangwiro ndi Mateyu :24, 5:24, kapena, Yohane Woyera 5:24, “Iye amene amva Mawu Anga, nakhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo wosatha; ndipo sadzafika ku chiweruzo, koma wadutsa kuchoka ku imfa wapita ku Moyo.” Osati chifukwa chakuti munali ndi kusuntha kulikonse, kugirigisha kulikonse; koma chifukwa chakuti inu mwakhala nawo mwayi wokhala ndi Khristu akuwululidwa kwa inu kuchokera Kumwamba, “Pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga.”

<sup>35</sup> Ndipo kenako, Yakobo, pamene iye anafa, mwana wake ananyamula thupi lake, ndipo iye anaikidwa mmanda limodzi ndi Abrahamu, Isaki, Sarah, ndi Yobu, mu Dziko Loyera, mu Palestina.

<sup>36</sup> Kenako, Yosefe, pokhala mneneri. Iye zinamuyendera bwino mu Igupto. Iye anamudziwa Mulungu. Mulungu anali atadziwulula Iyemwini kwa iye. Ndipo pamene iye anafa, anati, “Musadzaike mafupa anga kumusi kuno, koma mudzaike. . . pamene. . . Tsikulina Mulungu ndithudi adzakuyenderani inu!” Chifukwa chiyani? Iye anakhazikika mwaulemu pa Mawu a Mulungu kwa Mose, “Zaka foro handiredi iwo adzatumikira fuko lino, koma Ine ndidzawatulutsako iwo.” Iye anakhazikika mwaulemu pa Mawu.

<sup>37</sup> Ndipo ndi chofotokozera chokongola bwanji apa, ngati inu mungazindikire. M’hebri aliyense akamadutsa, ndi nsana wake wopenyedwa mpaka mkati, ndi oyang’anira akapolo. Ndipo pamene iye amayang’ana pa mafupa a mneneri wake, Yosefe, iye amadziwa tsikulina iwo adzatuluka. Pakuti, mafupa amenewo anasiyidwa kumeneko kwa chikumbutso, kuti tsikulina iwo akanadzatuluka.

<sup>38</sup> Izo zakhala pafupifupi zaka fifitini kapena eyitini zapitazo pamene Billy Paul, mnyamata wamng’ono wa pafupifupi usinkhu wa zaka faifi, zochulukira chomwecho ndithu. . . Iye tinali ndi duwa laling’ono limene ife timalitengera ku manda a amayi ake, pakutuluka kwa tsiku mmawa wina, pa Isitara, basi pamene dzuwa limatuluka, likusuzumira; kapena basi kusanache, zinali chomwecho, kenako nkumapita ku chiyanjano. Ndipo pamene ife tinali kuyenda kumapita ku manda, mnyamata wang’ono anavula chipewa chake pamene ife timayenda kupita kumene mchemwali wake wamng’ono ndi amayi ake anaikidwa. Ndipo iye anayamba kufwenthela ndi kumalira, ndipo iye anati, “Adadi, kodi amayi ali pansu pamenepo mu dzenje ilo?”

<sup>39</sup> Ine ndinati, “Ayi, mwana. Iwo sali pansu mu dzenje limenero. Iwo ali bwinoko mamilioni kuchulukitsa kuposa iwe ndi ine.”

Iye anati, “Kodi ine ndidzawawonanso amayi kenanso?”

<sup>40</sup> Ine ndinati, “Mwa chisomo cha Mulungu, ngati iwe ukukhumba zimenezo, iwe udzakhoza kuwawona iwo kenanso.”

Anati, “Kodi thupi lake lidzatuluka konse kuchokera mmanda awa?”

<sup>41</sup> Ine ndinati, “Wokonedwa, tseka maso ako, ndipo ine ndikuuza iwe kankhani kakang’ono. Zaka handiredi zambiri zapitazo, mmawa uno, kunali manda anasiyidwa apululu.” Ine ndinati, “Icho ndi chikumbutso kwa ‘iwo amene agona mwa Mulungu Khristu adzabwera Nawo pamene Iye azidzabwera.’” Popanda mthunzi wakukaikira, ine ndikukhazikika mwaulemu pa lonjezo Lamuyaya la Mulungu!

<sup>42</sup> Monga Yobu wakale, pamene ife timva kuti “phulusa ku phulusa, ndi fumbi ku fumbi,” izo zimandikumbutsa ine za Longfellow, amene anati:

Musati mundiuze ine, mwa ziwerengero za  
 chisoni,  
 Moyo ndi loto lopanda kanthu!  
 Ndipo moyo ndi wakufa umene umagona,  
 Ndipo zinthu siziri momwe izo zimawonekera.

Iye anati:

Eya, moyo ndi weniweni! Moyo ndi chikole!  
 Ndipo manda sindiwo mathero ake;  
 Pakuti fumbi iwe uli, ku fumbi udzabwerera,  
 Sanali kukamba za solo.

<sup>43</sup> Iwo amalitcha ilo la fiofane, kuti pamene ife tichoka kuno ife timapita kwinkwakwenso. Chirichonse chimene chingakhale, ine ndimatenga Mawu a mtumwi, pamene iye anati, “Ngati msasa wa pansi pano kapena malo okhalapo upasuka, ife tiri nawo wina ukudikirira, kuti tidzachoke kwa *wu* ndi kukalowa mwa Iwo.”

<sup>44</sup> Abrahamu, Isaki, Yakobo, Yobu, aneneri onsewo, iwo anali kudalira ndipo ankakhulupirira kuti kunali kubwera chiwukitsiro, kuti Muomboli anali kubwera. Iwo analosera za Iye. Enoki analosera za Iye; anapuma mwaulemu, anasindikiza umboni wake ndi izo. Isaki, Yakobo, Danieli, Yeremiya, Ezekieli, iwo ankakhazikika mwaulemu pa nthawi imene Mesiya akanati adzabwera.

<sup>45</sup> Ndipo iwo anafa ndipo miyoyo yawo inapita ku Paradiso. Iwo amalephera kupita mu Kukhalapo kwa Mulungu, chifukwa (ife tinali nazo izo usiku watha) kuti magazi a ng’ombe ndi mbuzi samatha kukhululukira machimo; iwo ankangophimba kokha machimo, kuyankhula za tsiku limene Nsembe yangwiwo; chifukwa magazi a chinyama samatha kubwerera kwa wopembedza, pakuti potero iye sibwenzi atasiya kumapereka nsembe za mtundu umenewo.

<sup>46</sup> Koma pamene Mwana wa Mulungu anafa, Moyo umene unali mwa Iye sunali uliwonse koma Mulungu, kuti adzabwererenso ndi kudzatitengera ife kukhala mu banja la Mulungu. Ndipo tsopano ife ndi ana a Mulungu, Moyo wochokera mu Magazi Ake.

<sup>47</sup> Tsopano zindikirani mwamsanga, pamene ife tikutsatira. Pamene mmbuyo mu Chipangano Chakale, ndi iwo amene ankakhulupirira ndipo amapembedza, ndipo amafera mu Chikhulupiro, kudikirira nthawi imeneyo. Chifukwa chimene aneneri amenewo ankachita zimenezo, ndipo ankafuna kuti adzaikidwe mmanda ku Palestina, iwo ankadziwa kuti chiukitsiro sichidzachitikira ku Igupto. Icho chimayenera kudzachitikira ku Palestina, basi.

<sup>48</sup> Ndi chifukwa chake ine ndikunena usikuuno: Ine ndiri nayo mitundu yonse ya maina; ine sindikusamala chimene anthu anganditche ine, izo sizimatanthauza kanthu kwa ine. Chinthu



chokhacho chimene ine ndikufuna kuti ndichite, ndi kudziwa ichi: kuti ine ndakhala wakufa, ndipo moyo wanga wabisika mwa Khristu, kupyolera mwa Mulungu, ndipo ndasindikizidwa ndi Mzimu Woyera; kuti pamene Iye azidzandiitana ine pakati pa akufa, ine ndidzayankha pa tsiku limenero. Mundiike ine mwa Khristu, pakuti iwo amene ali mwa Khristu Mulungu adzabwera nawo limodzi Naye pa tsiku limenero.

<sup>49</sup> Iye timalowa bwanji mwa Khristu? Akorinto Woyamba 12:13, “Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi, ndipo timadzakhala mbadwa limodzi za Ufumu wa Mulungu.” Iye timadzinenera kuti ndife amwendamnjira ndi alendo pa dziko lapansi lino, osatinso, ofunafuna zinthu za mdziko izi, koma kuyembekezera kubwera kwa Mfumu yodala kuti adzatenge ulamuliro, kuchokera ku nyanja kupita kunyanja yopanda malire, pamene Iye akubwera mu ulemelero Wake. Ndithudi, ife tikuyembekezera Kudza Kwake.

<sup>50</sup> Ndiyeno sindikukaikira mu mtima mwanga, koma ndicho chimene Yesu anali nacho mmalingaliro Ake pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, kunali kusalephera kumeneko kwa Mawu a Mulungu a Muyaya. Pakuti, ife tikudziwa kuti mwa Iye munali chidzalo cha Umulungu mu Thupi. Umulungu wonse unali mwa Iye. Iye anali zonse Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, koma zimakhala mu mawonekedwe a umunthu; fiofane ya Mulungu, chithunzi chachikulu cha Mulungu chimene Iye anamupangiramo munthu, kenako anadzamuika iye pa dziko lapansi. Iye anali ndi thupi. Mulungu sikuti alibe thupi. Mulungu ali nalo thupi, ndipo ilo limawoneka ngati munthu. Mose analiwona ilo, ena analiwona ilo, ndipo ilo limawoneka ngati munthu.

<sup>51</sup> Ndipo ndi chithunzi chabe, *ichi* chiri, cha chimene Icho chiri. Ndipo chirichonse pa dziko lapansi, kukongola, kukoma, kukongola kwa dziko lapansi, si china chirichonse pa dziko lapansi koma yankho kwa zabwinoko kuposa zimenezo, zimene zikutidikirira ife pamene ife tidzachoka pa dziko lino. Pakuti, chirichonse pa dziko lapansi ndi chitsanzo chabe cha chimene chiri Kumwamba. Chirichonse chimene chiri chabwino, chirichonse chimene chiri cholungama, chirichonse chimene chiri chokongola, mitengo, mbalame, chirichonse, ndi chitsanzo chabe cha chimene chiri Kumwamba.

<sup>52</sup> Moyo wathu womwe ndi chitsanzo chabe. Iwo ndi mthunzi chabe, ndipo osati chinthu chenichenicho. Iwo ndi mbali yongoimira. Zimatengera imfa kuti chithunzicho chipangidwe, kukatibwezeretsa ife mu fiofane kumene ife tinachokerako. Ndiye mu chiukitsiro ife tidzabwera mu mawonekedwe Ake, thupi lowukitsidwa. Ndi zokongola bwanji; osati kukongola kokha, koma ndi chenicheni, Choonadi chaulemu cha Mawu a Mulungu a Muyaya, kuti ife tidzakhala monga Iye.

<sup>53</sup> Zindikirani tsopano, Yesu, ali ndi mphamvu zonse za Mulungu, koma, pamene Iye anakumana ndi Satana, Iye sanagwiritse ntchito iliyonse ya mphamvu Zake. Iye anangolozera ku Mawu! Iye anatero. Iye anati, “Kwalembedwa, ‘Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu aliwonse otuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.’”

<sup>54</sup> Ndiye inu munganene bwanji kuti inu mukhoza kukhala kunyumba ndi kukhala Mkristu wabwino basi monga inu mukanakhallira ku tchalitchi? Inu simungakhoze kuchita zimenezo. Werengani Mawu! Mzimu Woyera umadya Mawu. Baibulo ndi chakudya chazimu cha Mulungu cha Mpingo Wake. Ndipo Mzimu Woyera ndi Iwowo Umene umawabweretsa Iwo kwa inu ndi kuwakhazikitsa Iwo mu mtima, ndipo mukamathokoza inu mumakhala mukuwathirira Iwo. Ndipo lonjezo lililonse la Umulungu lidzabereka ndendende basi chimene Mulungu ananena kuti likanadzachita. Ilo likuyenera kutero. Iwo ndi Mawu Ake, ndipo Iwo ndi Moyo.

<sup>55</sup> Tsopano, ine ndinaiwala kuti ine ndimayenera kungokhala ndi theka la ora. Izo zimanditengera ine nthawi yaitali kuti ndifike pa chimene ine ndikufuna kunena.

<sup>56</sup> Koma zindikirani Yesu mu ora lotsiriza, kapena awiri, a moyo Wake, ambiri, maulosi ambiri anakwaniritsidwa.

<sup>57</sup> Winawake ananena kwa ine, “M’bale Branham, *ichi* chikuyenera kuchitika, ndipo *icho* chikuyenera kuchitika.”

Ine ndinati, “Izo zikhoza kuchitika mu ora.”

<sup>58</sup> Ngati inu mungawerenge Masalmo 22, ndiyeno muwone ora Lake lakufa pa mtanda, Ine ndangoiwala tsopano ndi maulosi angati odziwika anakwaniritsidwa mu ma ora awiri kapena atatu a moyo Wake! Ndithudi, “Iwo anapyoza mapazi Anga ndi manja Anga. Mulungu wanga, Mulungu wanga, nchifukwa chiyani Inu mwandisiya Ine?” ndi zina zotero, monga Davide analirira izo.

<sup>59</sup> Ndiyeno chinthu china ine ndikufuna kuti inu muzindikire, Choonadi, gawo losalephera la Mawu a Mulungu. Baibulo linati, “Iye anasunga mafupa Ake onse, palibe limodzi la iwo linaswedwa.” Pakuti mu choimira, mwanawankhosa wa pasika anali woimira wa icho. Mwanawankhonsa akuyenera kukhala wopanda chilema, mafupa osweka sakuyenera kukhala mwa mwanawankhosa. Ndipo pa ora pamene Iye anali. . . Iye anali atafa, iwo anapita kukaswa miyendo Yake ndi nyundo. Ndipo basi asanati. . . Tayang’anani pa mphindi yovuta kwambiri iyo! Munthu amene anali ndi nyundo, atakonzekera kuti aswe miyendo Yake, koma Mawu a Mulungu anati, “Sipadzakhala fupa limodzi lidzaswedwe mu thupi Lake.”

“Kodi izo zidzachitika motani?” Ife tifikemo mofulumira.

<sup>60</sup> Mawu a Mulungu ndi Amuyaya! Ngati Mawu a Mulungu ndi angwiro chomwecho, iwo amene ali mwa Khristu ndi otsimikizika basi kuti adzauka chimodzimodzi monga mmene chiukitsiro chiripo. Mulungu ndi wokakamizidwa basi ku Mawu Ake, kuti akuchizeni inu, monga Iye ali woti akupulumutseni inu. Pakuti, Iye, iwo ndi Mawu Ake amene analonjeza zimenezo. Iwo ndi Mawu a Mulungu, ndipo ife tiribe ufulu wochotsera kwa Iwo. Koma basi kungoti, “Iwo ndi Choonadi.” Akhulupirireni Iwo! Ziribe kanthu kuti kukuchitika chiyani, akhulupirireni Iwo, mulimonse. Njira yake inali imeneyo yomwe ena onse a iwo ankeyenera kukhulupirira Iwo, ndipo ife sitikuchotsedwako kwa zimenezo. Mulungu anampereka Palestina kwa Israeli, koma iwo ankeyenera kumenyera inchi iliyonse ya nthaka imene iwo anaipeza. Lonjezolo ndi lanu, koma inu mukuyenera kumenyera inchi iliyonse imene inu mungaitenge; mdierekezi aziwona zimenezo, ndithudi iye adzatero.

<sup>61</sup> Koma zindikirani pamene iwo anakonzekera kuti athyole miyendo ya Ambuye wathu Yesu, ngati nyundo imeneyo ikanakantha mwendo ndi kuwuthyola iwo, Mulungu akanapezeka wabodza. Koma kunalibe adierekezi okwanira mu mdima wonse wozunza oti aloleze kuti nyundo imeneyo ikanthe thupi lofunika limenelo. Pakuti Davide, zaka eyiti handiredi zisanafike pamenepo, anati, “Sipadzakhala fupa limodzi lidzaswedwe mu thupi Lake.” Mawu a Mulungu akuyenera kuima Choonadi.

<sup>62</sup> Koma kodi iwo anachita chiyani ndiye? Iwo anatenga nthungo ndipo anaiyendetsa iyo mmbali Yake, ndipo Magazi ndi madzi anatuluka, kuti akwaniritse chimene Baibulo linanena, “Iwo anapyoza manja Anga ndi mmbali Mwanga.” Mawu anakwaniritsidwa.

<sup>63</sup> Tsopano pamene Iye anali kufa, oh, linali ora lowopsya bwanji! Ine ndikuganiza za nyimbo ija, ndipo, moonamtima, izo zimangondipangitsa ine kumverera moipa, pamene ine ndiganizira za nyimbo ija imene wandakatulo anailemba zaka zambiri zapitazo.

Pakati pa miyala yosweka ndi mlengalenga  
mwamdima,  
Mpulumutsi wanga anaweramitsa mutu Wake  
ndipo anafa;  
Chophimba chotsegulidwa chinawulula njira  
Zisangalalo za Mmiyamba ndi tsiku losatha.

<sup>64</sup> Ndipo pamene Iye anali atapachikidwa pamenepo, akuwukha magazi ndipo akufa, pamene Iye anaweramitsa Mutu wake, dzuwa linachita lokha manyazi kwambiri, kuyang’ana pansu pa zolengedwa zachivundi zimene Mulungu anazipanga mu chifaniziro Chake, amayenera kulipira mtengo wonga umenewo kuti aliwombole ilo, dzuwa linakana kuti liyang’ane

pansi padziko lapansi mu ora limenero. Mwezi unachita manyazi kwambiri mpaka iwo unachoka pa malo ake. Ndipo nyenyezi zinalozetsa nsana wawo kwa dziko lapansi. Ndi chinthu chowopsya bwanji tchimo likuyenera kuti linali, momwe Mulungu ankayenera kuti athane nalo ilo!

<sup>65</sup> Ndipo kuwawona ansembe onyoza amenewo, ndi malovu akulendewera pa nkhope Yake. Munthu anamumenya Iye pa mutu, ndi bango, ndipo anati, “Ngati Iwe uli Mneneri, tiuze ife ndani wakumenya Iwe.” Mmodzi wa iwo anamwetula ndevu pa nkhope Yake, ndipo anamumenya Iye pa nkhope, ndipo ankafuna kuti awone kuti Iye achita Nazo bwanji.

<sup>66</sup> Iye anati, “Ngati Ufumu Wanga ukanakhala wa dziko lapansi lino, Ine pomwepano ndikanawaitana Atate Anga, Iwo akananditumizira Ine gulu thwelofu la Angelo.”

<sup>67</sup> Izo zikanakhoza kusinthidwa, koma Iye akanachita bwanji izo? Iye basi sakanatha kuchita zimenezo, pakuti anali ana Ake omwe akulirira Magazi Ake. Kodi inu mungaganizire adadi, abambo, ana ake omwe (mu mdima) kumalirira magazi a bambo awo omwe? Ndi chifukwa chake Iye sakanatha kuchita chirichonse koma kufa. Ngati Iye sakanatero, chinakhala chiwonongeko kwa ana Ake, icho chikanakhala chiwonongeko kwa zolengedwa. Koma Iye ankayenera kuti afe, kuti apulumutse anthu Ake.

<sup>68</sup> Ndipo pamene Iye anatero, pamene Iye anaweramitsa mutu Wake, dziko lakale ili linali ndi tsemwe pansana pake. Liyenera kuti linali ndi kudzilambatitsa kwa kwa manjenje, pakuti Baibulo linanena kuti “dziko lonse, kuyambira ora la sikisi mpaka ora la naini, kunali mdima, unali pa nkhope yonse ya dziko lapansi.” Ndipo dziko lapansi linagwedezeka, ndipo miyala inang’ambika. Ndipo chinsalu cha mkachisi chinang’ambika kuyambira pamwamba kupita pansu; matabwa a nsembe anatembenezidwa. Mwana wa Mulungu wamoyo anafa. Iye anali atafa kwambiri mpaka kuti duzuwa linazindikira izo. Iye anali atafa kwambiri mpaka mwezi unazindikira izo. Iye anali atafa kwambiri mpaka nyenyezi zinazindikira izo. Iye anali atafa kwambiri mpaka dziko lapansi linazindikira izo. Iye anafa kwambiri mpaka ziwiya zinazindikira izo, mlengalenga munazindikira izo. Chirichonse chinkayenera kudziwa kuti ameneyo anali Mwana wa Mulungu! Pakuti, Mawu a Mulungu sangalephere, Iye analonjezedwa, kuchokera mmunda wa Edeni, “Mbewu imene ikanadzavulaza mutu wa serpenti.”

<sup>69</sup> Tsopano chinachitika chiyani kwa Iye? Iye anapita kuti pamene Iye anachoka pa mtanda ndi kupita ku manda a Yosefe wa Arimatheya?

<sup>70</sup> Iye anali wosauka kwambiri Iye analibe malo oti ayikepo mutu Wake. Iye anabadwira mu khola, ali ndi dzina loipa kumbuyo Kwake, monga “mwana wapathengo.” Iye

anasekedwa, anaseleulidwa, ananyozedwa, padziko lapansi. Iye anaseleulidwa, ndipo anakanidwa. Ndipo pamene Iye anafa, Iye amayenera kufa kudzera chilango cha imfa, pakati pa mbava ziwiri. Ndipo analibe ngakhale malo oti akamuike Iye, ndipo Iye anaikidwa mmanda a munthu wina. Mulungu kumene wa Kumwamba kubwera pa dziko lapansi! Kodi ife timaganiza kuti ndife ndani, kuti tikuyenera kuti tizidutsa mu mazunzo pang'ono? Chimene Iye anatichitira ife! Taganizani za zimenezo, mzanga, kawerengi zimenezo.

<sup>71</sup> Msilikari wa Chiroma anati, “Zoonadi, ameneyo ndi Mwana wa Mulungu.” Wochimwa anzindikira izo. Yudasi anati, “Ine ndapereka Magazi wosalakwa.” Iye anzindikira izo. Dziko lapansi lonse linazindikira izo.

<sup>72</sup> Kenako kodi Iye anapita kuti? Pamene munthu wafa, kodi izo zimathera pomwepo? Ayi, bwana. Iye ankayenera kuti afe mwanjira imeneyo chifukwa Baibulo la Mulungu linati Iye akanadzafa mwanjira imeneyo. Ndipo Iye amadalira Mawu a Mulungu. Ndi chifukwa chake Iye amatha kunena, mu moyo Wake, “Phwasulani kachisi uyu, ndipo Ine ndidzamuutsanso iye mu masiku atatu.”

<sup>73</sup> Pakuti Davide anati, malo amodzi, okha, mu Baibulo, pansi pa kuzodza, pamene Davide, munthu wa Mulungu, mneneri amene anzodzedwa ndi Mawu, anati, “Ine sindidzalola Woyera Wanga Uyo kuti awone chivundi, komanso sindidzawusiya moyo Wake mu hade.”

<sup>74</sup> Yesu anati, “Inu muphwasule thupi ili, ndipo Ine ndidzaliukitsanso ilo mu masiku atatu.” Iye ankadziwa kuti Mawu a Mulungu sangakhoze kulephera. Oh, mai!

<sup>75</sup> Ngati Iye akanapuma mwaulemu pa chimenecho, kukhulupirira kuti Mawu a Mulungu sangathe kulephera, ndi mochulukwa bwanji ife tingapume mwaulemu kuti ife tabadwanso mwatsopano mwa Mzimu Woyera, ndipo Iwo mboni mu mtima wathu tsopano kuti ife tikudziwa kuti Muomboli wathu ali moyo ndipo adzabweranso tsiku lina. Mukhale otsimikiza kuti iwo amene ali mwa Khristu Mulungu adzabwera nawo limodzi ndi Iye! Tsopano zindikirani.

<sup>76</sup> Ndi Uyo pamenepo. Iye ankadziwa kuti palibe khungu limodzi la thupi limene lidzawonongeke. Maora sevente thuu, chivundi chimalowamo. Ndi chifukwa chake Iye sanakhalemo masiku atatuwo. Iye anafa Lachisanu masana, anali atadzuka Lamungu mmawa. Koma, zinachitika mkati mwa masiku atatu amenewo. Mkati mwa masiku atatu amenewo Iye anali oti adzukanso, chifukwa Iye amadalira Mawu a Mulungu.

<sup>77</sup> Apa Iye akupita! Iye anakakhala kuti pamene Iye anachoka? Baibulo linati, “Iye anakwera. Iye anapita ndipo anakalalikira ku miyoyo imene inali mu ndende, imene siinalape mu kuleza mtima kwa masiku a Nowa.” Solo Yake, Mzimu Wake,

fiofane Yake ya umunthu Wake Womwe, zinapita kupansi. Tiyeni timutsatire Iye. Inu mungakonde kutero, usikuuno, kuti timutsatire Iye maminiti pang'ono? Tiyeni tiwone kumene Iye anapita.

<sup>78</sup> Kupansi kwa madera achivundi kuli mkombero wa mphamvu yaziwanda; pansi pake...pamwamba pake pali miyoyo ya osalungama; pansi pake ulamuliro omwe wa Satana, gehena. Kenako pamwamba pathu pomwe pali Mzimu Woyera; kenako pansi pa Guwa pali miyoyo ya anthu olungama; kenako ndi Mulungu Iyemwini. Wina akupita pansi, wina akukwera mmwamba; mizimu iwiri ili pano pa dziko lapansi, ikukopa anthu apa dziko lapansi lino.

<sup>79</sup> Ndipo pamene Yesu anafa, Iye anakwera mmwamba, pansi apo. Ine ndikukhoza kumuwona Iye Lachisanu masana amenewo, itachitika imfa Yake, [M'bale Branham akugogoda—Mkonzi]. akugogoda pa chitseko cha madera a otayika. Tiyeni timutsatire Iye miniti. Chitseko chikutseguka. Kunali akazi, kunali amuna, kunali atsikana achichepere, kunali okalamba, iwo ose anali pamodzi mmalo owopsya amenewo otchedwa ndende ya miyoyo yotaika.

<sup>80</sup> Ngati ine ndikanakhala nayo nthawi, ine ndikanakonda kuti ndikuuzeni inu. Ndipo awo mwina akhoza kungokhala masomphenya. Koma nthawi imodzi ine ndinapitako ku malo amenewo, ndipo ndinafuulira chifundo, pamene ine ndinali wochimwa ndikudutsa mu oparesoni. Pamene ine ndinatulukako, ine ndinali nditaima Kumadzulo, ndi manja anga nditakweza Mmwamba, ndi mtanda ukunyezimirira pa ine.

<sup>81</sup> Koma ku malo a chisoni amenewo, Yesu anadzafika pakhomo. Chirichonse chinkayenera kuti chichitire umboni kuti Iye anali Mwana wa Mulungu, chifukwa iwo anali atalalikiidwa mu kuleza mtima kwa masiku a Nowa. Akugogoda pa chitseko, Iye anati, “Ine ndi Iye Amene Enoki ankamukamba. Ine ndi Mbewu ya mkazi, imene inali yoti idzavulaze mutu wa serpenti. Mawu aliwonse a Mulungu akwaniritsidwa; Ine ndangofa kumene kutali pa Kalvare, ndipo Ine ndawugula Mpingo Wanga. Ndipo Mmodzi amene Enoki ankamukamba, Ndi Ineyo.” Ndipo iwo anali opanda chifundo, opanda chiyembekezo, chifukwa iwo anali atalakwa. Ndipo chitseko chinatsekedwa pamaso pawo.

<sup>82</sup> Kupita pansi mu dera la ziwanda! Mpaka pansi kupita ku zipata kumene za gehena! Iye akugogoda pa chitseko. [M'bale Branham akugogoda—Mkonzi].

<sup>83</sup> Apa ndi pamene Iye anali mmanda, thupi Lake liri, likudikirira chiukitsiro. Iye anayendera malo amene olungama ndi osalungama amapitako; kumene inu muti mudzapiteko limodzi la masiku awa, ku amodzi kapena malo enawo.

<sup>84</sup> Ndipo Iye akugogoda [M'bale Branham akugogoda—Mkonzi.] pa chitseko cha gehena. Ndipo, pamene Iye anatero, mdierekezi anadzatulukira. Ndipo ine ndikukhoza kumumva iye akuti, “Oh, chotero potsiriza Iwe wafika. Ine ndithudi ndimaganiza ndathana Nawe pamene ine ndinamupha Abele.”

<sup>85</sup> Inu mwaona, pamene Mbewu imeneyo inalonjezedwa mmunda wa Edeni, mdierekezi wayesera mowirizika kuwononga Mbewu imeneyo. Ndipo imfa ya Abele, ndi kubwera kwa Seti, inali basi imfa, kuikidwa mmanda, ndi chiukitsiro cha Khristu. Mbewu imeneyo ikuyenera kupitirira. Ndipo iye anayesetsa kuti ayiwononge Iyo.

<sup>86</sup> Iye anati, “Ine ndimaganiza ine ndathana nawe Iwe pamene ine ndinamuwononga Abele. Ine ndimaganiza ndathana nawe Iwe pamene ine ndinawononga aneneri. Ine ndinali wotsimikiza kuti ine ndathana nawe Iwe pamene ndinamudula mutu Yohane. Koma tsopano, zitachitika zonsezo, Iwe wafika. ine ndakupeza Iwe tsopano.” Oh, Mai!

<sup>87</sup> Ine ndikukhoza kumumva Iye akuti, “Satana, bwera kuno!” Iye ndi Bwana tsopano. Akumufikira, akutenga mafungulo awo a imfa ndi gehena kuwachotsa pa mbali yake, akuwapachika iwo pa mbali Yake Yomwe. “Ine ndikufuna kuti ndiike chidziwitso pa iwe. Iwe wakhala wa chinyengo kwa nthawi yokwanira. Ine ndi wobadwa mwa namwali Mwana wa Mulungu wa Moyo. Magazi Anga adakali onyowa pa mtanda, ndipo ngongole yonse yalipiridwa! Iwe ulibe maufulu panonso. Wavulidwa. Ndipatse Ine makiyi amenewo!” Uko nkulondola. Akutembenuka ndipo akumupatsa iye theche labwino lathanzi, ndikumenyetsa chitseko pamodzi, ndikuti, “Ukhale mmenemo! Ine ndi bwana kuyambira pano mpakana.”

<sup>88</sup> Tsopano, Iye analibe mafungulo a ku Ufumu, chifukwa Iye anawapereka iwo kwa Petro; ife tinazipeza zonsezo mmawa, mu ubatizo wa mmadzi. Koma iye anali ndi mafungulo a imfa ndi gehena, ndipo Iye anawatenga iwo; chitachitika chiukitsiro Chake, Iye anati, “Ine ndiri nawo mafungulo a imfa ndi gehena.” Petro anali ndi mafungulo a ku Ufumu. Satana anali nawo mafungulo a imfa ndi gehena; koma tsopano Yesu wawatenga iwo, Iye ndi Bwana.

<sup>89</sup> Apa Iye akuyamba. Iyo ikufika ku Isitara; nthawi ikupita mofulumira. Koma pali gulu lina. Yobu ali kuti? Abrahamu ali kuti? Ali kuti iwo? Ali kuti anthu aja amene amadalira Mawu a Mulungu? Kodi Iye wawaiwala iwo? Kodi imfa inawafaniza iwo? Kodi izo zinali zonse za izo? Ayi, ayi; Mulungu akuyenera kusunga Mawu Ake.

<sup>90</sup> Ine ndikukhoza kumuwona Iye. Tiyeni tisuzumire pang'ono mu Paradiso, ndikuyang'ana cha kumeneko. Ndipo ine ndikumuwona Sarah ndi Abrahamu akuyenda yenda kumeneko, ndipo patapita kanthawi [M'bale Branham

akugogoda—Mkonzi.] chinachake pa chitseko. Abrahamu akupita ndikukatsegula chitseko, anati, “Wokonededwa, bwera kuno. Tayang’ana kuno! Tayang’ana kuno, uyo ndi Mmodzi yemwe uja amene anaima ndi ine pansi pa mtengo wa thundu tsiku lijali.” Iye ndi Mulungu wa Abrahamu.

<sup>91</sup> Basi pomwepo ine ndikukhoza kumuwona Danieli akuyang’ana pa phewa lake, ndipo akuti, “Ilo ndi Thanthwe limene linadulidwa kuchokera m’phiri, motsimikiza basi monga momwe ine ndaimira pano.”

<sup>92</sup> Ine ndikumuwona Yobu akudzuka, akuti, “Uyo ndi Muwomboli wanga amene ine ndinati ine ndikudziwa ali moyo, ndipo tsikulina Iye akanadzaima pa dziko lapansi. Thupi langa mwinamwake silingakhale koma supuni yaing’ono yozadza ndi phulusa, koma mu maminiti fifitini kuyambira tsopano ine ndidzakhala mmenemo kenanso. Ndi Iyeyo.”

<sup>93</sup> Ezekieli akuyang’ana pamwamba, ndipo anati, “Ine ndinamuwona Munthu yemweyo ngati Gudumu mkati mwa Gudumu, likuzungulira, kutali mmwamba mkati mwa mpweya.” Oh, mai!

<sup>94</sup> Kenako pakubwera Enoki. Enoki anati, “Ine ndinamuwona Iye akubwera ndi masauzande teni a oyera Ake, kuti adzapereke chiweruzo.”

<sup>95</sup> Pamenepo panali oyera a Chipangano Chakale akudikirira, ndithudi iwo anali, pansi pa chitetezero cha magazi. Iwo samatha kupita mu Kukhalapo kwa Mulungu, Mulungu wa Kumwamba, chifukwa magazi a mbuzi ndi nkhoa samatha kuchotsa tchimo.

<sup>96</sup> Koma Iye anati, “Abale anga, ine ndi Mmodzi amene inu mukuganiza Ine ndiri. Ine ndine Mbewu ya mkazi. Ine ndi Mwana wa Davide. Ine ndi Mwana wa Mulungu. Ine ndi wobadwa mwa namwali Uja. Magazi Anga atetezera izo. Inu munadikirira pansi pa magazi a nkhoa ndi mbuzi, koma tsopano Magazi Anga akutetezera, ndipo inu ndi mfulu. Tiyeni tikwere mmwamba, Isitara ikuyandikira.” Tangoganizani, izo zinali basi pafupifupi zaka naintini handiredi chakuti zapitazo, usikuuno.

<sup>97</sup> Ine ndikukhoza kumumva Abrahamu akuti, “Ambuye, ife tikakafika mu thupi lathu kenanso; ndipo Sarah ndi ine timangozikonda izo mwabwino kwambiri; kodi Inu mungadandaule ngati ife titaima pang’ono, mokhala ngati, pa njira Yanu?”

<sup>98</sup> Chabwino, ine ndikutha kumumva Iye akuti, “Bwanji, ayi, ndithudi ayi. Ine ndikhala ndi ophunzira Anga kwa pafupi masiku forte. Akuyang’anayang’ana ndipo akuwona momwe chirichonse chikuwonekera!”



<sup>99</sup> Mmawa wa ulemelero wa Isitara uja (umene ife tidzautenge mmawa, Ambuye akalola) pamene Iye anawuka kwa akufa, Baibulo linati, molingana ndi Mateyu Woyera 27, kuti “Ambiri a oyera amene anagona mu fumbi la pa dziko lapansi, anadzuka ndipo anatuluka mmanda.” Anali ndani amenewo? Abrahamu, Isaki, Yakobo, Yobu, iwo amene mwa vumbulutso lowululidwa mwauzimu anadziwa kuti Muomboli akanadzaima pa dziko lapansi tsiku lina. Ndi iwowo, zipatso zoyamba za iwo amene anagona. Kumeneko iwo anayenda mu mzinda. Ine ndikukhoza kumuwona Sarah ndi Abrahamu, achichepere, ndipo ozadza ndi...ndi owoneka bwino, ndi—ndi ozadza ndi moyo, osadzakalambanso, osadzadwalanso, osadzamvanso njala, akuyendayenda mu thupi lawo.

<sup>100</sup> Kayafa ataima pamenepo, akuti, “Inu mukudziwa chiyani? Panali chinachake chinachitika tsiku lina, tangoyang’anani kuipa kumene kachisi uyu alimo! Apo pali...Ife tikuyenera kupeza winawake kuti asoke katani imeneyo. Tawawonani awo, mabokosi a nsembe agudubuzidwa. Chinachitika ndi chiyani? Kodi Munthu ameneyo anali mkasidi? Kodi Iye anali mfiti? Kapena, chinachitika ndi chiyani? Anati! Bwera kuno, Josephus, banja laling’ono laima apo ndi ndani?”

Abrahamu anati, “Sarah, ife tazindikiridwa. Ife kulibwino tichokepo.”

<sup>101</sup> “Anawonekera kwa ambiri!” Izo sizinali zonse za izo. Potseka, penyani. Tsiku lina pamene Iye anali atatha... iwo anayendera; Abrahamu, Isaki, Yakobo, ndi onse a iwo anali atayendera dziko la kwawo. Pamene Yesu anakwera mmwamba...

<sup>102</sup> Inu mukuti, “M’bale Branham, kodi izo ndi nthano?” Ayi, bwana! Ine ndikuwonetsani inu mu Malemba, mu miniti.

<sup>103</sup> Pamene Iye anayamba kukwera mmwamba, iwo anangomuwona Iye yekha, koma oyera a Chipangano Chakale anapita limodzi ndi Iye, pakuti Baibulo linanena kuti “Iye anatsogolera amsinga ku msinga, ndipo anapereka mphatso kwa anthu.” Ndipo ine ndikukhoza kumuwona Iye pamene Iye akukwera mmwamba, ndipo akulumikizana ndi mpingo Wake.

<sup>104</sup> Angelo awiri kuchokera pa gulu limene limaimba nyimbo, anabwerera pamenepo, ndipo anati, “Amuna inu a ku Galileya, chifukwa chiyani inu mwaima ndi kumayang’ana mmwamba? Pakuti Yesu yemwe uyu, amene anatengedwera mmwamba adzabwereranso.” Ndithudi! Iwo anathamanganso kubwerera kuti akakhale nawo pa mdipitiwo.

<sup>105</sup> Ndipo pansu kudutsa mu mlengalenga Yesu ndi oyera a Chipangano Chakale anapita. Iwo anadutsa mwezi, iwo anadutsa dzuwa, iwo anadutsa nyenyezi. Ndipo pamene iwo anakafika powona Miyamba yaikulu, yokongola yoyera imeneyo, oyera a Chipangano Chakale anafuula, akubwereza

Lemba, “Kwezani mmwamba, inu zipata zosatha, ndipo inu mukwezedwe mmwamba! Kwezani mmwamba, inu zipata zosatha, ndipo mukwezedwe mmwamba! Ndipo mulole Mfumu ya Ulemelero ilowe mkati!”

<sup>106</sup> Angelo onse anasonkhana mmwamba pamwamba pa zigwiriro za Kumwamba, ndipo anati, “Nndani Mfumu ya Ulemelero iyi?”

<sup>107</sup> Oyera a Chipangano Chakale anati, “Ambuye wa makamu, wamphamvu mu nkondo! Iye anali Mgonjetsi!”

<sup>108</sup> Mngelo anakanikiza batani lalikulu, ndipo zipata za ngale zinatseguka.

<sup>109</sup> Kutsika kudutsa mu Mzinda wa Yerusalemu anabwera wamkulu, Mgonjetsi wamphamvu, akubweretsa oyera a Chipangano Chakale. Bandi ya Angelo ikuimba, pamene Angelo amafuula. Iye anali Mgonjetsi wamphamvu! Iye anali ndi mafungulo a imfa ndi gehena akulendewera pa mbali Pake, akupita kumadutsa nyumba zachifumu za Ulemelero mpaka Iye anakafika ku Mpandowachifumu. Ndipo Iye anati, “Atate, ndi awa apa. Iwo anakhulupirira, mu chikhulupiriro pa Mawu Anu, kuti ine ndidzabwera tsikulina. Ine ndagonjetsa ziwiri zonse imfa ndi gehena.” Chinali chiyani chimenecho, m’bale? Iye anali ndi zipsyera mdzanja Lake, kuwonetsera kuti Iye anali mu nkondo. Ulemerero kwa Mulungu Mmwambamwamba! Iye ndi Mgonjetsi wamphamvu ameneyo! “Ndi awa apa, Atate; Abrahamu, Isaki, ndi Yakobo.”

<sup>110</sup> Ine ndikukhoza kumumva Iye akuti, “Mwana, kwera pamwamba apa kumbali Yanga, ndipo ukhale pansu kufikira Ine nditapanga mdani aliyense popondapo mapazi Ako.” M’bale, tsikulina Iye adzabweranso, ndipo lidzakhala tsiku bwanji limenelo!

<sup>111</sup> Iye sanangokhala phee pamene Iye anali mmanda. Ife timaganiza kuti Iye anangogona mmenemo, wakufa. Koma Iye anali pansu akugonjetsabe, Iye anapita pansu ndipo anakalanda mafungulo kuchokera kwa Satana, Iye ali ndi mafungulo a ziwiri zonse imfa ndi gehena, usikuuno. Iye anati, “Chifukwa Ine ndiri moyo, inu mukhoza kukhala moyo, nanunso.”

<sup>112</sup> Ine ndikudabwa usikuuno, m’bale wanga wokonedwa, mlongo, kodi inu mwaziganizira izo moona mtima? Kodi inu mukuzindikira kuti inu mumangokhala moyo chifukwa chakuti Iye ali moyo? Kodi inu mwayamikira izo mokwanira kuti mukadzipereke nokha, ndikuti, “Mulungu, ndine pano, wochimwa, ndichitireni chifundo ine”? Kodi inu munayamba mwavomerezapo Nsembe yokwanira mu zonse imeneyo? Inu munayamba mwamuwuzapo Iye kuti inu mumamukonda Iye? Kodi zimapweteka kumverera kwanu pamene inu muchita cholakwika? Ngati inu simunayambe mwafikapo ku chokuchitikirani chimenecho tsopano, mu kuikidwa mmanda

uku! Pamene, nthawi yathu ikutha. Basi mukungomverera bwino! Koma, ine ndikudabwa, ngati inu simunayambepo mwalandira Khristu ngati Mpulumutsi wanu wanu, Ine ndikudabwa ngati inu mungachite zimenezo pamene ife tikuweramitsa mitu yathu mphindi chabe mu mawu a pemphero.

113 Imbani iyo, *Pakati Pa Miyala Ikusweka*, ngati inu mungathe, Mlongo Gertie, ngati inu muli nayo iyo. Chabwino, iliyonse itithandiza.

114 Ndi mitu yanu yoweramitsidwa, ine ndikufunsani inu funso loona mtima kwenikweni. Kumbukirani abwenzi, wochimwa kapena woyera, inu sikuti basi zatha pamene ife tikuikani inu mmanda. Solo yanu ili kwinkwaka. Tsopano, Yesu anakayendera malo awiri onsewo, molingana ndi Malemba. Iye angakakupezeni inu kuti ngati inu mutapita usikuuno? Kodi mukapeza chitseko cha chifundo chitasekedwa mukuwona, chifukwa inu mwamukana? Kumbukirani, Iye si Mpulumutsi kokha, Iye ndi Woweruza. Inu ndi oweruza tsopano, inu mumamuweruza Iye chotani? Mulole Iye akhale Mpulumutsi wanu tsopano.

115 Nkhani yaing'ono imabwera mmalingaliro mwanga. Nthawi ina kalelo mnyamata wamng'ono anali atakhala mu—mu ngolo. Mfuti inawombera pansu mu msewu, ndipo akavalo anathawa, iye anali akuwoloka phiri. Mnyamata wamng'ono woweta ng'ombe anathamanga ndipo anaimitsa akavalo ngolo isanawoloke phiri, chifukwa iyo inali itanyamula mwana. Iye anapulumsa moyo wa wamng'onoyo.

116 Zaka zambiri zitachitika zimenezo, ataima mu nyumba ya mlandu. Mnyamata yemweyu anapalamula mlandu, anatenga njira yolakwika, analakwa. Iye amamwa mowa, amachita njuga, anamuwombera munthu; ndipo analakwa, anapezeka wolakwa. Ndipo woweruza anadzuka ndipo anati, “Ine ndikukulumulira iwe kuti ukadzinyonge pakhosi lako mpaka moyo wako wachivundi utapita.”

117 Mnyamatayo anati, “Woweruza!” Ndipo iye anasokoneza dongosolo la mu khoti, pamene iye anadumphira mu njanji ndipo anakagwera pa mapazi a woweruza, kufuna chifundo. Iye anati, “Woweruza, tayang'anani nkhope yanga! Kodi inu simukundidziwa ine?”

Iye anati, “Ayi, mwana, ine sindikukudziwa.”

118 Iye anati, “Inu mukuwukumbukira moyo wa mnyamata winawake wamng'ono umene inu munawupulumutsa, zaka zambiri zapitazo, kuchokera ku kavalo wothawa?”

Iye anati, “Inde, ine ndikukumbukira zimenezo.”

119 Iye anati, “Ine ndi mnyamata ameneyo.” Iye anati, “Oweruza, inu munandipulumutsa ine nthawi imeneyo. N dipulumutseni ine tsopano!”

120 Woweruza anayang’ana pansu pa iye, ndipo anati, “Mwana, tsiku limene lija ine ndinali mpulumutsi wako. Lero ndine woweruza wako.”

121 Lero Iye ndi Mpulumutsi wako, wochimwa, mawa Iye akhoza kukhala Woweruza wako. Tiyeni tiganizire izo tsopano, pamene nyimbo ikuyimba. Ndipo aliyense akupemphera, iwo amene ali pa mabwalo a pemphero ndi Mulungu.

122 Ine ndikudabwa usikuuno tsopano, mwamsanga, iwo amene angakonde kumuvomera Khristu ngati Mpulumutsi wawo, munene, “Mulungu, ndichitireni ine chifundo, wochimwa. Ine ndikufuna kubwera mwa Magazi okhetsedwa. Ine ndatopa ndikujowina mipingo ndi kuthamanga kuchoka malo awa kupita malo awa. Ine ndikufuna kubadwanso mwatsopano. Ine ndikufuna chondichitikira mu mtima mwanga kuti ine ndizidziwa kuti Khristu wadziulula Iyemwini kwa ine, mwa vumbulutso lauzimu limene inu mwangoyankhula kumene, M’bale Branham. Ine ndikufuna vumbulutso lauzimu, Mzimu Woyera mu mtima wanga, kundipanga ine kukhala wamoyo, kumubweretsa Khristu kukhala weniweni kwa ine kusiyana ndi momwe ine ndiliri kwa inemwini. Ine ndikukhumba chondichitikira chimenecho, M’bale Branham. Kodi inu mundipempherera ine pamene ine ndikukweza dzanja langa?” Inu mungakweze dzanja lanu tsopano, inu amene mukufuna kuti mukumbukiridwe. Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitseni inu kumbuyo uko, dona. Izo nzabwino. Mulungu akudalitseni inu, bwana. Izo nzabwino. Kwezani manja anu, tsopano dzikwezani mmwamba dzanja lanulo.

123 Inu mungakhale bwanji wamanyazi? Inu mungakane zangati Zimenezo, mzanga? Kumbukirani.

124 “Oh,” inu mukuti, “M’bale Branham, alaliki alalikira kwa zaka.” Ine ndikudziwa, koma limodzi la masiku awa iwo adzasiya kulalikira. Ndipo momwe zinthu zikuwonekera, izo zikhoza kukhala pomwe pano. Inu mudzamvera ulaliki wanu wotsiriza. Kunena moona, uwu ukhoza kukhala wotsirizira wanu.

125 “Oh,” inu mukuti, “Ndine wachichepere.” Izo ziribe kanthu. Imfa siimalemekeza munthu, kapena usinkhu kapena kuthekerera.

126 Kodi inu tsopano mumuvomereza Iye ngati Mpulumutsi wanuwanu, pokweza dzanja lanu, ndikuti, “Mulungu, mundichitire ine chifundo?” Mukweze manja anu ndi ena onse awa, ndipo munene kuti, “Tsopano ine ndikufuna kumuvomereza Khristu.” Kodi inu mungakweze dzanja lanu mmwamba?

<sup>127</sup> Winawake yemwe wabwerera mmbuyo, anene kuti, “Mulungu, mundichitire ine chifundo. Ine ndikufuna kuti ndibwerere kwa Khristu usikuuno, kuti mawa likhoza kukhala chiukitsiro, chatsopano, kwa ine.” Kodi inu mungakweze manja anu? Bweretsani mmwamba dzanja lanulo, ndikuti, “Mundichitire ine chifundo. Ine ndikufuna kuti ndibwere tsopano.” Kodi inu mungachite zimenezo? Kwezani mmwamba dzanja lanulo, munene, “Ine ndakhala wobwerera mmbuyo, koma usikuuno. . .” Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitseni inu. Izo nzabwino. “Ine ndimuvomereza Khristu ngati Mpulumutsi wanga wanga. Ine ndimuvomereza Iye usikuuno. Ine ndayendayenda, zaka zambiri kuchoka kwa Mulungu, koma tsopano ine ndikubwera kwathu.” Kodi inu mumuvomereza Iye usikuuno, kuti ichi chikakhale chiukitsiro chatsopano kwa inu, moyo wanu wakale ukakhoze kutha?


<sup>128</sup> Dona uyu akubwera ku guwa, kuti adzapange kulapa kwake, kuti adzaimo. Wina wakenso akufuna kuti atenge malo awo apa, bwerani kumtunda kuno ndi iye, pa kuvomereza kwawo? Kodi inu mungaimirire, ndi kubwera ku guwa, nanunso. Guwa ndi lotseguka. Ndithudi. Bwerani kumtunda kuno, pomwe pano. Ngati inu mukufuna kuti mudzaimo pano ndi kupemphera, izo zikhala zabwino basi. Bwerani. Mungabwere? Pa kuvomereza kwa chikhulupiriro chanu, pa chikhulupiriro chanu mwa Mwana wa Mulungu, kodi inu mungabwere tsopano? Chabwino.

<sup>129</sup> Izo ziri ndi inu, inu mukukumbukira. Inu ndi inuyo. Kodi ndinu wochimwa? Kodi ndinu wobwerera mmbuyo? Kodi inu ndi wozizira muli kutali ndi Khristu? Ndipo inu mukufuna kuti muukitsidwe mwatsopano ndi Iye tsopano, kuyamba moyo watsopano? Nanga bwanji inu, mwamuna ndi mkazi amene mwakhala pa—mwakhala mosakhazikika kwa nthawi yaitali, kukangana mnyumba mwanu? Kodi inu simubwera ndi kudzakonza chinthu chimenecho ndi Mulungu ndi wina ndi mzake tsopano? Mupange Isitara kukhala Isitara yeniyeni kwa inu, kuyamba khomo latsopano.

<sup>130</sup> Nanga bwanji inu amene simunakhalepo, simunakhalepo ndi pemphero mnyumba mwanu, inu mumangopita kunyumba mukachoka ku tchalitchi ndi kuyesetsa kukhala mwabwino mmene inu mungathere, osabweretsa banja pamodzi kuti mupemphere? Ndi chifukwa chake ife tiri ndi kupanda makhalidwe kwa achinyamata ndi zinthu zimene ife tiri nazo. Ndi chifukwa chake makomo a Achimerica ali osweka. Kodi inu simubwera, muyambe mwatsopano usikuuno? Kodi inu muchita zimenezo? Inu mukuitanidwa. Kumbukirani, ndine mtumiki wanu tsopano; ine ndidzakhala mboni pa tsiku limenero.

Pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa, ndiye, tsopano ku pemphero.

<sup>131</sup> Atate athu Odala Akumwamba, usikuuno ife tikubweretsa kwa Inu omvetsera awa, mu ulemu wopatulika kwambiri umene ife tikuudziwa. Ife modzichepetsa tikuyandikira Mpando Wanu wachifumu. Ndipo utatha Uthenga usikuuno, umene, kuikidwa mmanda kopambana kuja, Iye sanangogona chete, solo Yake inapitirira kupita ku madera ndi kukamalizitsa ntchito ya Mulungu, imene Iye anazodzedweratu kuti adzaichite. Ndipo mawa mmawa, ife tidzapeza kumene Iye anadutsa mmadera mmwamba, akugonjetsa chirichonse, mu chiukitsiro Chake. Koma Iye anadzatulukira mmawa wa Isitara ku kulungamitsidwa kwathu. Ndipo ife tikupeza kuti Iye anatumiza Mzimu Woyera kuti ubwerere, kuti udzawatsutse anthu a tchimo.

<sup>132</sup> Ndipo ife tikupemphera usikuuno, Ambuye, kuti iwo amene anakweza manja awo akumbukiridwe pamaso Panu. Mulole chisankho chawo chikhale chochokera mu mtima mwawo usikuuno, kuti iwo akulandirani Inu, ndipo akukhulupirirani Inu, ndipo mulole iwo asindikizidwe ndi Chisindikizo cha lonjezo usikuuno, Mzimu Woyera. Perekani izi, Atate. Pakuti, ife tikuwapereka iwo kwa Inu, ndi Uthenga uwu usikuuno. Mulole Iwo ukawadalitse iwo amene amvetsera Iwo, iwo, Ambuye, amene ati awutengere Iwo limodzi nawo kunyumba kwawo, ndipo mukauzamtse Iwo mwakuya mmitima mwawo. Mulole iwo akakhale moyo pa Mawu a Mulungu. Perekani izi, Atate, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Khristu. Ameni. 

*KUIKIDWA MMANDA* CHA57-0420  
(The Entombment)

MAULALIKI A CHITSITSIMUTSO CHA ISITARA

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Loweluka madzulo, Epulo 20, 1957, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2021 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)